-Ngati mukumvera Mawu a Mulungu, mudzaphunzira m'mene mungayithaŵire Nyanja ya Moto Wosatha.

-Mulungu akufuna kuti inu mudzimvera Mawu a Mulungu.
-Satana sakufuna kuti inu mudzimvera Mawu a Mulungu.

-Ndikuyembekezera kuti inu mudzimvera Mawu a Mulungu.



PHUNZIRO LA 11

-Pachiyambi, kodi Adamu ndi Hava amkakhala kuti?
-M'munda mwa Edeni.

-Kodi Adamu ndi Hava amkakhala bwanji m'munda mwa Edeni?
-Adamu ndi Hava amkakhala mosangalala kwambiri m'munda mwa Edeni.

-Kodi chifukwa chiyani Adamu ndi Hanva amkakhala mosangalala kwambiri?
-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava amkamumvera Mulungu.
-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava anali ndi zinhu zonse zimene amkazifuna.

-Kodi nanga Satana, mdani wa Mulungu anali kuti?
-Satana amkamuwona Mulungu pamene Iye amkamulenga Adamu ndi Hava.

-Satana anadziwa kuti Mulungu walenga Adamu ndi Hava mu chifaniziro chake ndipoanakwiya kwambiri.

-Satana anadziwa kuti Mulungu wamupatsa Adamu udindo woyang'anira dziko lonse la pasi ndipo iye anakwiya kwambiri.

-Satana amamuda Mulungu.
-Satana anadziŵa kuti iye sangathe kumugonjetsa Mulungu.

-Chomcho, Satana anaganiza zomugonjetsa Adamu ndi Hava.
-Chomcho, Satana anaganiza zomuwononga Adamu ndi

Hawa.

-Kodi mukuganiza kuti Satana anayesa bwanji kumuwononga Adamu ndi Hava?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 3:1

1-Pa nthaŵi imeneyo njoka inali yochenjera kwambiri kuposa nyama zonse zimene analenga Ambuye Mulungu. Njoka ija inamufunsa mkaziyo kuti, “Kodi ndi zowona zakuti Mulungu anati kuti usadye chipatso kuchokera mu m’mtengo wina uliwonse wa m’munda muno?”

-Kodi njoka imene imkalamkhulana ndi Hava inali yeniyeni?
-Iyayi.

-Kodi amene amkalamkhulana ndi Hava weniweni ndi ndani?
-Satana.
-Satana analowa mwa njoka.

-Kodi chifukwa chiyani Satana analowa mwa njoka?
-Chifukwa chakuti amkazibisa yekha.

-Satana anabisala mkati mwa njoka chifukwa chakuti amkafuna kumukodwetsa Hava.
-Satana anabisala mkati mwa njoka chifukwa chakuti amkafuna kumunamiza Hava.
-Satana anabisala mwa njoka chifukwa chakuti amkafuna kumuwononga Hava.

-Apa pali chitsanzo:

-Kodi mulenje akafuna kupha nyama ya mtchire, amabisala kuti ayiphe nyamayo?



-Poyamba, Adamu ndi Hava anali amzake a Mulungu.
-Tsopano, Adamu ndi Hava anali adani a Mulungu.

-Poyamba, Adamu ndi Hava anali ana a Mulungu.
-Tsopano, Adamu ndi Hava anali ana a Satana.

-Poyamba, Adamu ndi Hava amkayenda ndi Mulungu.
-Tsopano, Adamu ndi Hava amkabisala kwa Mulungu.

-Poyamba, Adamu ndi Hava amkamutsatira Mulungu.
-Tsopano, Adamu ndi Hava amkamubisala Mulungu.

-Poyamba, Adamu ndi Hava samkalidziwa tchimo.
-Tsopano, Adamu ndi Hava amkalidziwa tchimo.

-Pachiyambi, Adamu ndi Hava analibe manyazi.
-Tsopano, Adamu ndi Hava anali ndi manyazi.

-Kodi mukuganiza kuti ndi chifukwa chiyani Satana anamunamiza Adamu ndi Hava?

-Chifukwa chakuti Satana amamuda Mulungu, iye amayesayesa kuwononga ntchito ya Mulunguyo.
-Chifukwa chakuti Satana amaŵada anthu onse, iye amayesayesa kwawononga anthu onse.
-Satana safuna kuti munthu wina aliyense amvere Mawu a Mulungu.
-Satana safuna kuti munthu wina aliyense akhulupilire mwa Mulungu.

-Satana amafuna kuti anthu onse apite ku Nyanja ya Moto Wosatha.
-Satana amafuna kuti inu mupite ku Njanja ya Moto Wosatha.

-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava anamutsatira Satana, iwowo anasanduka kukhala adani a Mulungu.

-Kodi chinachitika ndi chiyani Adamu ndi Hava atamulakwira Mulungu?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 3:7-8

7-Atangotha kudya, maso awo anatseguka, ndipo anazindikira kuti anali maliseche; chomcho anasoka masamba a mkuyu ndi kuvala.

8-Madzulo dzuŵa litapepa, aŵiriwo anamva mtswatswa, Ambuye Mulungu amkayenda m'mundamo, ndipo iwo anabisala mkatikati mwa mitengo kuti Ambuye Mulunguwo asaŵawone.

-Kodi Adamu ndi Hava atalakwa, anazindikira chiyani?
-Anazindikira kuti anali maliseche.

-Adamu ndi Hava atalakwa, kodi anachita chiyani atazindikira kuti anali maliseche?
-Anasoka zovala za masamba.

-Adamu ndi Hava atalakwa, kodi anachita chiyani atamva mtswatswa wa Mulungu akubwera kudzaŵawona iwowo?

-Anabisala kuti Mulungu asawawone.

-Kodi ndi kotheka kubisala kwa Mulungu?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani sikuli kotheka kubisala kwa Mulungu?
-Mulungu ali palipose.



-Inde.

-Kodi chimachitika ndi chiyani akapanda kubisala?
-Sangaphe nyama ya ntchireyo.

-Satana anabisala kuti amukodwetsa Hava, ngati m'mene amabisalira mulenje akafuna kupha nyama.

-Kodi Satana amayesa kwakodwetsa ndi kumawanamiza anthu masiku ano?
-Inde.

-Kodi Satana amayesa bwanji kumawakodwetsa ndi kuwanamiza anthu masiku ano?

-Choyamba, Satana amalamkhula ndi ife m'maganizo athu.
-Kachiŵiri, Satana amalamkhula ndi ife kupitila mwa anthu ena.
-Kachitatu, Satana amalamkhula ndi ife kupitila mu ziwanda.

-Choyamba, Satana amalamkhula ndi ife m'maganizo athu.

-Nthaŵi zina Satana amayika maganizo m'mitu mwathu.

-Timaganiza kuti maganizo amenewo ndi athu, koma amakhla maganizo amene Satana wayika mwa ife.

-Satana adzakuwuzani inu kuti musamakhulupilire Mawu a Mulungu.

-Maganizo amenewo sakhala ochokera kwa Mulungu.
-Maganizo amenewo amayikidwa mwa inu ndi Satana.

-Kachiŵiri, Satana amalamkhula kwa ife kupitila mwa anthu

ena.

-Anthu ena akhoza kukuwuzani inu kuti musamamvere mawu a Mulungu.
-Maganizo amenewo siwochokera kwa Mulungu.

-Maganizo amenewo ndi maganizo amene Satana wayika mwa anthu ena.

-Anthu ena adzakuwuzani inu kuti, “Ife tili ndi zikhulupiliro zathu.”
-“Chomcho ife sitikuzifuna zikhulupiliro zatsopanozi.”

-Maganizo amenewo siwochokera kwa Mulungu.
-Maganizo amenewo ndi maganizo amene Satana wayika mwa anthu ena.

-Kachitatu, Satana amalamkhula ndi ife kupitila mu ziwanda.

-Ziwanda zinalankhula kwa makolo athu.
-Ziwanda zimkawawuza makolo anthu kuti adziwawotcha ana awo pa moto, ndipo iwo amkapanga zimenezo.

-Maganizo amenewo siwochokera kwa Mulungu.
-Maganizo amenewo ndi maganizo amene anayikidwa mwa makolo anu ndi Satana ndi ziwanda zake.

-Kodi Hava anadziwa kuti amkalankhulana ndi Satana?
-Iyayi.

-Hava samkadziwa kuti anali Satana amene amkalankhulana nayeyo.
-Chifukwa chakuti Satanayo ankazibisa yekha.





6 Mkaziyo atawuwona kuti mtengowo unali wokongola, ndipo zipatso zake ziyenera kukhala zokoma kudya, iye anayamba kuzikhumbira zipatsozo kuti adye, kuti akhale wa mzeru. Chomcho mkaziyo anathyola zipatso zina za mu mtengowo ndipo anadya. Ndipo anatenganso zina kukamupatsa mamuna wake, ndipo iyenso anadya.

-Satana anamunamiza Hava ndipo Havayo anamukhulupilira Satanayo.

-Hava sanamumvere Mulungu, ndipo anadya chipatso.
-Adamunso sanamumvere Mulungu, ndipo iyenso anadya chipatso.

-Adamu ndi Hava anamumvera Satana.
-Adamu ndi Hava sanamumvere Mulungu.

-Adamu ndi Hava anamulakwila Mulungu.

-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava sanamumvere Mulungu, iwo anasanduka kukhala adani a Mulungu.
-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava anamumvera Satana, anasanduka kukhala adani a Mulungu.

Apa pali chitsanzo:

-Kodi ngati mzako wakuwukira ndi kuyamba kucheza ndi mdani wako amene amkafuna kukupha iweyo, mzakoyo sakhalanso mdani wako?
-Akhala mdani wako.

-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava anamuwukira Mulungu, iwowo anasanduka kukhala adani a Mulungu.

-Mulungu.

-Satana ankati kuti zimene ananena Mulungu zinali zona-ma.
-Satana amkamutcha Mulungu kuti anali wabodza.

-Kodi china ndi chiyani chimene Satana anamuwuza Hava kuti chidzawawonekera akadzadya chipatso kuchokera mu Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa?
-Satana anati kuti iwowo adzakhala ngati Mulungu.

-Kodi anthu angakhale ngati Mulungu?
-Iyayi.
-Mulungu yekha ndi Mulungu.

-Satana amkanama pamene anamuwuza Hava kuti adza-khala ngati Mulungu.

-Pachiyambi, Satana sanamumvere Mulungu.
-Tsopano, Satana amkafuna kuti Hava asamumvere Mulungu.

-Mulungu sanaŵalenge anthu kuti adzikhala ngati m'mene anthu amanenera.
-Mulungu anaŵalenga anthu kuti adzikhala ngati m'mene Mulungu akunenera.

-Mulungu sanaŵalenge anthu kuti adzikhala malingana ndi malalamulo awo.
-Mulungu anaŵalenga anthu kuti adzikhala malingana ndi malamulo a Mulungu.

-Kodi Mukuganiza kuti Hava anachita chiyani?
-Kodi Hava anamumvera Mulungu kapena Satana?



-Makolo anu samkadziwa kuti anali Satana amene amkalamkhula kwa iwowo.

-Chifukwa chakuti Satana amkazibisa yekha.
-Satana anazibisa yekha kuti amukodwetse ndi kumunami-za Hava.
-Satana anazibisa yekha kuti aŵakodwetse ndi kuŵana-miza makolo anu.

-Kodi chifukwa chiyani Satana amkafuna kumukodwetsa ndi kumunamiza Hava?

-Chifukwa chakuti Satana samkamukonda Hava.
-Chifukwa chakuti Satana amkafuna kumuwononga Hava.

-Kodi chifukwa chiyani Satana amafuna kumaŵatchela ndikumaŵanamiza makolo anu?

-Chifukwa chakuti Satana amadana ndi anthu onse.
-Chifukwa chakuti Satana akufuna kuwononga anthu onse.

-Tiyeni tiŵerengenso funso limene Satana anamufunsa Hava:

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 3:1

1-Njoka ija inamufunsa mkaziyo kuti, "Kodi ndi zowona zakuti Mulungu anati kuti usadye chipatso ku-chokera mu m'mtengo wina uliwonse wa m'munda muno?"

-Kodi chifukwa chiyani Satana anamufunsa Hava funso li-meneli?

-Satana anali atazidziŵa kale zimene analankhula Mulun-gu.

-Satana anali atazidziwa kale zimene Mulungu anaŵawuza iwowo kuti asadye chipatso kuchokera mu Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Satana anafunsa funso limeneli?

-Satana anafunsa funso limeneli ndi cholinga chofuna kumukodwetsa Hava.
-Satana anafunsa funso limeneli ndi cholinga chofuna kumunamiza Hava.
-Satana anafunsa funso limeneli ndi cholinga chofuna kumuwononga Hava.

-Tiyeni tiŵerenge kuyankha kwa Hava:

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 3:2-3

2-Mkaziyo anayankha kuti,"Tikhoza kudya zipatso zochokera m'mitengo yonse ya m'munda muno,
3-koma Mulungu anati, "Musadye chipatso kuchokera mu Mtengo umene uli pakati pa mundawu, ngakhalenso kuwugwira, chifukwa chakuti mukatero, mudzafa."

-Mulungu sananene kuti Adamu ndi Hava asakhuze chipatsocho.

-Mulungu anangoti kuti Adamu ndi Hava asadye chipatso.

-M'buku la Mulungu, timaŵerenga zakuti Mulungu anamulamula  Adamu yekha kuti asadye chipatso.
-Koma lamulo la Adamu lili lamulonso la Hava.

-Ngakhale kuti Mawu a Mulungu analembedwa kwa anthu a zaka zambiri zapitazo, Mawu a Mulunguwo anatilembelanso ife.



-Uthenga wa Mulungu kwa anthu akuda ndi azungu ndi ofanana.

-Uthenga wa Mulungu kwa Acheŵa ndi Ayao ndi ofanana.

-Uthenga wa Mulungu kwa anthu onse ndi ofanana.

-Uthenga wa Mulungu wa dzulo, lero mpaka kalekale uli chimodzimodzi.

-Kodi inu mukuganiza kuti Satana anamuyankha Hava?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 3:4-5

4-Koma njokayo inati kwa mkaziyo, "Iyayi, kufa simudzafa konse."
5-Mulungu akudziŵa kuti inu mukadzadya zipatso zimenezi, maso anu adzatsekuka, ndipo mudzakhala monga m'mene alili Mulunguyo."

-Kodi Mulungu anamuwuza Adamu kuti chidzaŵachitikira chiyani akadzadya chipatso kuchokera mu Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa?
-Adzafa.

-Kodi nanga Satana anamuwuza Hava kuti chidzaŵachitikura chiyana akadzadya chipatso kuchokera mu Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa?
-Satana anamuwuza Hava kuti sadzafa akadzadya chipatso.

-Kodi mukuganiza kuti amene amkanena zowona ndi ndani, Satana kapena Mulungu?